Zimene Mungachite Ngati Bambo Kapena Mayi Anu Atayamba Kudwala

Ngati bambo kapena mayi anu ali ndi matenda aakulu komanso otenga nthawi yaitali, tsambali lingakuthandizeni kudziwa zimene mungachite kuti muwasamalire komanso kuti inuyo muzidzisamalira

1 MUKAMASAMALIRA **BAMBO KAPENA MAYI** ANU



Kodi bambo kapena mayi anu amadwala matenda anji?

_____

Kodi matendawo amawalepheretsa kuchita chiyani?

_____

_____

_____

Ngati amalephera kuchita zinthu zina, mungawathandize bwanji?

ZIMENE AMALEPHERA KUCHITA	MMENE MUNGAWATHANDIZIRE
_____	_____
_____	_____
_____	_____
_____	_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Sankhani ntchito zapakhomo zimene mungagwire

Mungachite chiyani kuti muwathandize kuti asamakhale ndi nkhawa kwambiri?

Zochita

‘Muziwamvera chisoni.’ (1 Petulo 3:8) Muyenera kumvetsa mmene bambo kapena mayi akumvera chifukwa cha matendawo. Mwachitsanzo, mtsikana wina dzina lake Ellen ananena kuti: “Zaka zapitazi, ndinachita zinthu zingapo zofunika zomwe ndimalakalaka mayi anga akanakhalapo koma analephera kupezekapo. *Ngati zimandikhudza choncho kuti mayi anga sanapezekepo, ndikuganiza kuti iwowo zimawakhudza kwambiri kuposa ineyo.”*

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 ZIMENE MUNGACHITE KUTI **INUNSO** MUZIDZISAMALIRA

Gregory ananena kuti: “Mayi anga anagonekedwa kuchipatala kwa nthawi yaitali ndipo nthawi yonseyo ndinkakhala ndekha kunyumba. Koma atapezako bwino n’kuwatulutsa, ankavutikabe chifukwa cha mankhwala amphamvu omwe ankamwa. Sizinali zophweka kuti ndizitha kusamalira mayi anga pa chilichonse.”

Kodi ndi vuto lalikulu liti lomwe mumakumana nalo mukamasamalira bambo kapena mayi anu?

_____

_____

Kodi mungatani kuti muzisamalira thanzi lanu?	Mungatani kuti musamakhale ndi nkhawa kwambiri?	Nanga mungatani kuti ubwenzi wanu ndi Mulungu ukhalebe wolimba?
ZIMENE MUKUFUNA KUCHITA:	**ZIMENE MUKUFUNA KUCHITA:**	**ZIMENE MUKUFUNA KUCHITA:**
_____	_____	_____
_____	_____	_____
_____	_____	_____
_____	_____	_____
ZIMENE MUYENERA KUPEWA:	**ZIMENE MUYENERA KUPEWA:**	**ZIMENE MUYENERA KUPEWA:**
_____	_____	_____
_____	_____	_____
_____	_____	_____
_____	_____	_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

ZOMWE ZINGAKUTHANDIZENI

Baibulo limati: “Bwenzi lenileni limakukonda nthawi zonse, ndipo bwenzilo ndi m’bale amene anabadwira kuti akuthandize pakagwa mavuto.” (Miyambo 17:17) Lembani mayina a anthu awiri omwe mungawadziwitse ngati mutafuna kuti akuthandizeni.





Baibulo limati: “Umutulire Yehova nkhawa zako, Ndipo iye adzakuchirikiza. Sadzalola kuti wolungama agwedezeke.” (Salimo 55:22) Mogwirizana ndi mfundo ya palembali, ndi zinthu ziti zomwe muyenera kuzipempherera?

_____

_____

_____

_____

Zochita

Lembani malemba angapo omwe mumaona kuti amakulimbikitsani. Ellen, yemwe tamutchula kumayambiriro kwa nkhaniyi ananena kuti: “Tsiku lina ndinawerenga lemba la Yesaya 46:4 lomwe limanena kuti, ‘Ine sindisintha ngakhale kwa wokalamba, ndipo munthu wa imvi ndimamunyamula nthawi zonse. Ndithu ineyo ndidzachitapo kanthu kuti ndiwatenge, ndiwanyamule ndi kuwapulumutsa.’ Lembali limandithandiza kudziwa kuti ineyo komanso mayi anga sitili tokha. Yehova adzatithandiza pa vuto lililonse lomwe tingakumane nalo.”

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania